**EXAMINATION NO:________________________________**

# NCHALO ZONE EXAMINATION BOARD

## 2021 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE MOCK EXAMINATIONS

## CHICHEWA

(MALIKISI 100)

DATE:____/_______/___________

TIME ALLOWED:_______________

**Dzina lanu: ____________________________________________________________________________**

**Dzina la sukulu lanu: _____________________________________________________________________**

**MALANGIZO**

1. Onetsesani kuti pepala ili ndi masamba
   Osindikizidwa Khumi ndi imodzi
2. Pepala ili ndi magawo **A, B, C**, ndi **D**
3. Lembani dzina la sukulu lanupa mwamba pa
   Tsamba ilililonse
4. Lembani nambala ya mayeso pa mwamba pa
   Tsamba ililonse
5. Lembani chimangilizo kapena kalata mu **G**
6. **awo A**,
   Ndipo muyakhe mafunso onse mu **Gawo B, C,** ndi **D**
7. Lembani yakho lanu mu **Gawo A** pa mapepala omwe
   Ali kumathero kwa ma funso one Gawoli
8. Yakhani mafunso a mun **Gawo B** ndi C m'mipata
   Yomwe yapelekedwa pansi pa funso lililonse
9. Yakhani mafunso a **Gawo D** pozunguliza lembo lokhoza
   Pafunso lililonse
10. Muchitebulo chili pamwambachi onetseni funso lililonse
    Lomwe mwayakha pochonga mubokosi lomwe
    ilikutsogolo
    Kwake
11. Perekani kwa okuyang'anirani kulemba mayeso
    (imvijireta)
    Pepala lonseli nthawi ikakwana

| **Funso** | **Chongani zomwe mwayakha** | **Muno musalembemo** | |
|---|---|---|---|
| **1** | | | |
| **2** | | | |
| **3** | | | |
| **4** | | | |
| **5** | | | |
| **6** | | | |
| **6-10** | | | |
| **11-15** | | | |
| **16-20** | | | |
| **21-35** | | | |
| **26-30** | | | |
| **31-35** | | | |
| **36-40** | | | |
| **41-45** | | | |

## GAWO A (Malikisi 30

**Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani mutu wa chimangirizo kapena wa kalata. Mawu a Chimangirizo chanu kapena kalata yanu asachepere 100 koma asabzole 150.**

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu:

   **CHITUKUKO CHA M'DERA LATHU**

   Mwa zina tsatani izi polemba chimangirizo chanu.

   **Ndime yoyamba**

   - Ndi chitukuko chanji chomwe chili m'dera lanu?
   - Chitukukochi chinabwera liti?
   - Ndi midzi iti yomwe ikutengapo mbali pa chitukukocho?

   **Ndime yachiwiri**

   - Chitukukocho ndi chofunika bwanji m'deralo?
   - Ndondomeko yomwe yatsatidwa kuti chitukuko chibwere?

   **Ndime yachitatu**

   - Fotokozani kufunika kotengapo mbali pa chitukuko
   - Nanga chitukukocho mukuchisamalira bwanji. Fotokozani.

**KAPENA**

2. Lembani kalata yomufotokozera mnzanu zomwe mudzachite mukadzamaliza sukulu. Mwa zina tsatani izi polemba:

   **Ndime yoyamba**

   - Ntchito yomwe mukufuna kudzagwira.
   - Cholinga chosankha ntchitoyo

   **Ndime yachiwiri**

   - Ndi maphunziro anji omwe angakuthandizeni kudzagwira ntchito imeneyo?
   - Zomwe mudzachite mukadzayamba ntchito imeneyo

   **Ndime yachitatu**

   - Ndi malangizo ati omwe mungapereke kwa anzanu omwe akufuna kudzagwira ntchito yomwe mwasankhayo.

________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
________________________________________________________________________________
__________________________________________________________________________

## GAWO B (Malikisi 20)

## KUMVETSA NKHANI

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenako yankhani mafunso otsatirawo.

### UFUMU WA A MAKEKOWA

Kalekale m'mudzi mwa Makekowa mudali mnyamata wotchedwa Petani.
Mudzi umenewu udali pakati pa phiri la Mbongozi ndi nkhalango yaikulu yotchedwa Manyani. M'nkhalangomu mudali mikango yomwe imagwira anthu ndi zifuyo.

Petani adali muphwa wamkulu wa mfumu Makekowa. Mfumu Makekowa idali yomveka kwambiri chifukwa cha nzeru zake zolosera. Mfumuyi idali ndi mkondo wake womwe sinkausiya ikakhala pa ulendo. Anthu amati mkondowu udali ndi mphamvu za uzimu zomwe zimathandiza kusunga bwino mudzi uja. Mkondowu udali wakale zedi ndipo amaupereka kwa amene amayembekeza kulowa ufumu, mfumu ikadzala chinangwa.

Mfumu Makekowa itamwalira, anthu adasankha Petani kuti akhale mfumu. Pakuti tsoka likalimba amayamba ndi garu wako kukuluma, mkondo uja udasowa tsiku lolonga Petani ufumu lisadakwane. Amene adazembetsa mkondo uja adali Katema, mbale wa Petani. Katema adabisa mkondo uja chifukwa cha nsanje. Mkondowu adakaubisa kutali kwa mfumu Mtayamanja. Katema adachita izi podziwa kuti Petani sakadalowa ufumu popanda mkondo uja.
Popeza mkondo udali ndi mphamvu za azimu, mfumu Mtayamanja adalota mfumu Makekowa akumuuza kuti akaubweze. Kutacha mmawa, mfumu Mtayamanja idakapereka mkondowo kwa akuluakulu a m'mudzi mwa Makekowa. Mfumu Mtayamanja idafotokoza kuti Katema ndiye adakausungitsa kwa iyeyo. Zitatero, Petani adamulonga mfumu ndipo Katema adathawa m'mudzimo napita kutali popeza adadziwa kuti zimenezi ndizochititsa manyazi. Kumene adathawirako adalibe mtendere pozindikira kuti choipa chitsata mwini. Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.

**MAFUNSO.**

a. Kodi kwawo kwa Petani kudali kuti?

______________________________________________________________________

_____________________________________________________(1 Mark)

b. N'chifukwa chiyani nkhalango ya Manyani idali yoopsya?

______________________________________________________________________

_____________________________________________________(2 Marks)

c. N'chifukwa chani mfumu Makekowa idali yomveka? (1 malikisi)

______________________________________________________________

d. Kodi nchifukwa ninji mfumu Makekowa siimasiya mkondo wake?

______________________________________________________________________

___________________________________________________________(2 malikisi)

e. Pelekani matanthauzo amau awa

i. "Dzala chinangwa"

________________________________________________

ii. "Kulosela"

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

f. Ndi yani amalandila mkondo mfumu ikamwalila? ( 2 malikisi)

______________________________________________________________________

_______________________________________________________

g. N'chifukwa chani katema adabitsa mkondo? Pelekani zifukwa ziwili. (2 malikisi)

________________________________________________________

h. Pezani mkuluwiko m'nkhaniyi womwe ukutanthauza kuti "tsoka umachoka nalo pakhomo pako pomwe"

___________________________________________________ (2 malikisi)

i. Perekani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi mawu awa:

   i. "bisa"_____________________________________ (1 malikisi)

   ii. "tsuka"____________________________________ (1 malikisi)

j. N'chifukwa chiyani katema adathawa m'mudzimo?

____________________________________________________ (2 malikisi)

k. Lembani zinthu zomwe zikadachitika akadakhala kuti mfumu mtayamanja sadabweze mkondo uja. _______________________________________________________ (2 malikisi)

## GAWO C (MALIKISI 10)

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo

"Mfumu, ine ndafika ndi dandaulo, mwana wa a Bango ndinampeza dzulo akuba mbwanda m'munda mwanga."

i. Ndi malonje anji akuperekedwa m'kankhanika?

_________________________________________________________________ (1 malikisi)

ii. Ndani akuyankhula m'kankhanika?

_________________________________________________________________ (1 malikisi)

iii. Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi woti "mbwanda"

_________________________________________________________________ (1 malikisi)

B. Lembani udindo wa munthu yemwe amathandizira mfumu m'mudzi.

_________________________________________________________________ (1 malikisi)

C. Perekani kuipa kumodzi kochotsa zikwangwani za pamsewu.

_________________________________________________________________ (1 malikisi)

5. Kupanga ziganizo

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. Sungulumwa_____________________________________________________________

_________________________________________________________________________

b. Ngakhale_______________________________________________________________

___________________________________________________________

c. Osati__________________________________________________________________

_________________________________________________________________________

d. Moseketsa______________________________________________________________

e. Mlendo_________________________________________________________________

_________________________________________________________________________

## GAWO D (MALIKISI 40)

Zungulizani lembo lokhoza (A,B,C kapena D) m'mafunso otsatirawa

Mafunso **6** mpaka **10**: sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

6. Jenifa <u>wapita</u> kale kuchigayo.
   a. Dzina
   b. Mneni
   c. Mperekezi
   d. Muonjezi
7. <u>Kalanga ine!</u> Mwana uja wagwera pamwala.
   a. Mfuwu
   b. Dzina
   c. Mfotokozi
   d. Muonjezi
8. Utenge ichi <u>osati</u> icho
   a. Mulumikizi
   b. Dzina
   c. Mpelekezi
   d. Mfuwu
9. <u>Mpingo</u> wathu ndi wabwino kwambili
   a. Mvekelo
   b. Mfotokozi
   c. Dzina
   d. Muonjezi
10. Akuyenda <u>mofulumira</u> kwambili
    a. Dzina
    b. Muonjezi
    c. Mfotokozi
    d. M'neni

Mafunso 11 mpaka 15: sankhani mitundu ya alumikizi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

11. Stella wagula mpunga <u>ndi</u> mbale.
    a. Wa mneni
    b. Wa dzina
    c. Wa mfotokozi
    d. Wa muonjezi
12. Mwana wa ulemu <u>ndi</u> wanzeru amasangalatsa a phunzitsi
    a. Wa dzina
    b. Wa muonjezi
    c. Wa mneni
    d. Wa mfotokozi
13. Felix ana bwera <u>ndipo</u> wapita
    a. Wa muonjezi
    b. Wa dzina
    c. Wa mneni
    d. Wa mfotokozi
14. Mwana wanga akugwira ntchito mwamphamvu <u>ndi</u> mwa luso
    a. Wa muonjezi
    b. Wa dzina
    c. Wa mfotokozi
    d. Wa mneni
15. Mphatso wajambula <u>ndi</u> kulemba magawo a chiwala
    a. Wa dzina
    b. Wa muonjezi
    c. Wa mfotokozi
    d. Wa mneni

Mafunso 16 mpaka 20: sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikilo zoyenera za mkalembedwe

16.

a. Hehede! zoseketsa ndi wodwala omwe

b. Hehede, zoseketsa ndi wodwala omwe.

c. Hehede! zoseketsa ndi wodwala omwe.

d. Hehede! zoseketsa ndi wodwala omwe?

17.

a. Kodi ukulemba, chiyani nyani iwe?

b. Kodi ukulemba chiyani, nyani iwe?

c. Kodi, ukulemba chiyani nyani iwe?

d. Kodi ukulemba chiyani? nyani iwe.

18.

a. Ndampandira m'nyumba ntakwiya.

b. Ndam'pandira m'nyumba n'takwiya.

c. Ndam'pandira mnyumba ntakwiya.

d. Ndam'pandira mnyumba ntakwiya.

19.

a. Abambo akuti, amayi anu apita kumadzi

b. Abambo akuti "amayi anu apita kumadzi"

c. Abambo akuti, "amayi anu apita kumadzi."

d. "Abambo akuti," amayi anu apita kumadzi.

20.

a. Iye wagula nsomba, nthochi ndi anyezi.

b. Iye wagula nsomba, nthochi, ndi anyezi

c. Iye wagula nsomba nthochi, ndi anyezi.

d. Iye, wagula nsomba nthochi ndi anyezi.

Mafunso 21 mpaka 25; sankhani mitundu ya misintho ya aneni omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

21. Mkazi wachiwerewere <u>waphetsa</u> mwamuna.

a. Wochitidwa

b. Wom'chitika

c. Womchititsa

d. Wonyazitsa

22. Alinafe <u>amubera</u> zovala

a. Wochititsitsa

b. Womchitira

c. Wochitidwa

d. Wochitirana

23. Anyamata <u>ang'ambirana</u> zovala

a. Wochitidwa

b. Wochitirana

c. Wochitika

d. Wochititsitsa

24. Iye <u>wamasula</u> thumba lija

a. Wam'chitira

b. Wochititsa

c. Wochitidwa

d. Wotsutsa

25. <u>Usamadutsadutsa</u> nsewu njinga zingakugunde.

a. Wochititsitsa

b. Wochititsa

c. Wobwereza bwereza

d. Wotsutsa

**Mafunso 26 mpaka 30; sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zosayima pazokha zomwe ziri ndi mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi;**

26. Wezi wawerenga buku lomwe adagula dzana
    a. Ya dzina
    b. Ya mfotokozi
    c. Ya muwonjezi
    d. Ya mlowa mmalo
27. Amayi amuphikira phala mwana amene akudwala
    a. Ya dzina
    b. Ya mfotokozi
    c. Ya muwonjezi
    d. Ya mlowa mmalo
28. Yohane akuyenda ngati akuvina.
    a. Ya mfotokozi
    b. Ya muwonjezi
    c. Yoyima pa yokha
    d. Ya dzina
29. Sindilowa pokhapokha mutasesamo m'nyumbamo.
    a. Ya mfotokozi
    b. Ya dzina
    c. Ya muwonjezi
    d. Yoyima payokha
30. Sizowona kuti abwera lero.
    a. Ya muwonjezi
    b. Ya mfotokozi
    c. Yoyima payokha
    d. Ya dzina

**Mafunso 31 mpaka 35. Sankhani chachikazi cha mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazo**

31. Iwo ndi ndoda yolangiza bwino ana
    a. Mayi
    b. Mchemwali
    c. Mtegwa
    d. Ntchembere
32. Iwo sakumufuna mkamwini wawo
    a. Mtengwa
    b. Mkaweni
    c. Mpongozi
    d. Mkwatibwi
33. Aphiri agula tonde wakuda
    a. Msoti
    b. Thazi
    c. Mkota
    d. Nsidzi
34. Chipsolopsolo cha a Bengo chasowa
    a. Msoti
    b. Mkota
    c. Mkazi
    d. dona
35. muphwa uja abwera lero
    a. mkota
    b. mfumakazi
    c. mchemwali
    d. mkazi

**mafunso 36 mpaka 40. Sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo mziganizo zotsatirazi.**

36. Ana achedwa kusukulu.
    a. Mu-, Mi-
    b. Mu-, A-
    c. Ka-, Ti
    d. U-, ma-
37. Amayi agula maungu okoma kwambiri.
    a. Li-, Ma
    b. Mu-, Mi
    c. Ka-, Ti
    d. I-, Zi
38. Mkango wagwira mbuzi.
    a. Li' Ma-
    b. Mu-, A-
    c. Mu-, Mi
    d. Chi-, Zi
39. Sukulu yathu ndiyokongola.
    a. Li-, ma-
    b. I-, zi
    c. Chi-, zi
    d. U-, ma-
40. Kudambwe kuli zilombo
    a. U-, ma-
    b. Ku-pa-, mu
    c. Chi-, zi
    d. Li-, ma-

**Mafunso 41 mpaka 42 sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi**

41. M'yang'ana dzuwa adasochera
    a. Ukapeza mwayi ugwiritse ntchito
    b. Ukamutchula munthu ndiye kuti akubwera
    c. Ndibwino kufunsa ngati sitikudziwa
    d. Taya mwayi wopezapeza
42. Zengerezu adalinda kwawukwanu
    a. Sibwino kuchita zinthu mozengereza kapena mopanda changu
    b. Ndibwino kunena zomwe wabwerera
    c. Sibwino kukhulupirira zakale zokha
    d. Sibwino kukometsa munthu wolakwa poweruza.
43. Watchera kumwezi khanga zaona.
    a. Munthu ukachita zopanda pake manyazi amagwira iwe
    b. Kuchita chinyengo chomwe pambuyo pake chimafika poululika
    c. Nthawi zina ngalu amachita zabwino
    d. Tisamadane ndi zinthu zomwe palibe.

**Mafunso 44 mpaka 45 sankhani mawu amene akufanana m'matanthauzo ndi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi**

44. Mayi Tembo amalima mawere.
    a. Nsawa
    b. Nandolo
    c. Mapira
    d. Lipoko
45. Tizikwirira mapesi kuti aziwolerana mokwanira
    a. Azivundirana
    b. Azilowerana
    c. Azisakanizana
    d. Azimwazikana

# END OF QUESTION PAPER